CANDIDATE NUMBER: ______________________________

# CENTRAL EAST EDUCATION DIVISION

## 2023 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION MOCK EXAMINATIONS

## CHICHEWA

Monday, 27th March

Subject Number: M032/II

Time Allowed: 2 hours

(1:00 p.m.-3:00p.m.)

**PAPER II**

**(Malikisi 90)**

| Question Number | Tick if answered | Do not write in these columns | |
|---|---|---|---|
| **1** | | | |
| **2** | | | |
| **3** | | | |
| **4** | | | |
| **5** | | | |
| **6** | | | |
| **7** | | | |
| | | | |

**Malangizo**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi limodzi.**
2. **M'gawo A:** Malamulo a Chiyankhulo: Yankhani mafunso **onse. (Malikisi 40)**
3. **M'gawo B:** Kumvetsa Nkhani: Yankhani mafunso **onse. (Malikisi 20)**
4. **M'gawo C:** Chifupikitso **(Malikisi 15)**
5. **M'gawo D:** Chimasuliro **(Malikisi 15)**
6. Lembani **dzina lanu kapena nambala** pamwamba pa tsamba **lililonse loyankhirapo.**
7. Muchitebulo chilli pambalichi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
8. Perekani pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana.

**@ 2023 CEED MOCK**

**TURN OVER!**



Downloaded for ***FREE*** from *www.kizitochikuni.com* - For more info: *contact@kizitochikuni.com*

**CANDIDATE NUMBER: ________________________________**

**Gawo A** (Malikisi 40)

**Malamulo a Chiyankhulo**

**Langizo:** Yankhani mafunso **onse.**

**1.** a. Pangani aonjezi ndi mawu otsatirawa.

(i) chinunu________________________________

(ii) nong'ona________________________________

(iii) tali________________________________

(iv) nyengerera________________________________**(Malikisi 4)**

b. Tchulani mitundu ya kanenedwe ka aneni omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

(i) Khalani chete nonsenu.

________________________________

(ii) Ndakhuta kwambiri.

________________________________

(iii) Tiwerenge kwambiri kuti tikhoze bwino.

________________________________

(iv) Muyende bwino.

________________________________

(v) Adakolola zambiri atathira manyowa ndi fetereza.

________________________________

(vi) Kamakandayu adabwera liti?

________________________________

**(Malikisi 6)**

**2.** a. Pangani mvekero **m'modzi** wamchitidwe ndi **mmodzi** wamkhalidwe kuchokera ku mneni aliyense wa awa:

(i) gona

wamchitidwe:

________________________________

wamkhalidwe:

________________________________



Downloaded for ***FREE*** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

(ii) thifuka

wamchitidwe:

________________________________________

wamkhalidwe:

________________________________________

**(Malikisi 4)**

b. Perekani zitsanzo za agwirizanitsi a mitundu ili m'munsiyi m'ziganizo ndipo mutseke mzere kunsi kwa agwirizanitsiwo.

(i) Mgwirizanitsi wamchitidwantchito

________________________________________

**(Malikisi 2)**

(ii) Mgwirizanitsi wowerengera

________________________________________

**(Malikisi 2)**

(iii) Mgwirizanitsi wamgwirizano

________________________________________

**(Malikisi 2)**

**3.** a. Kodi **'li'** ali ndi mzere kunsi kwake m'ziganizo zotsatirazi akugwira ntchito yanji?

(i) Khandali <u>li</u>kudwala kwambiri.

________________________________________

(ii) Khasu<u>li</u> mwalibunthitsa.

________________________________________

(iii) Bukuli mu<u>li</u>samale.

________________________________________

(iv) M'phiri ili mu<u>li</u> mizimu.

________________________________________

**(Malikisi 4)**



Downloaded for ***FREE*** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

CANDIDATE NUMBER: ______________________________

b. Tsekani mzere kunsi kwa akapandamneni m'ziganizo zotsatirazi ndipo mupereke mitundu yawo.

(i) Iye ndi mnzakeyo adakondana koposa.

**mtundu:**

______________________________

(ii) Bwanji mukuseka mokhadzula kukamwa?

**mtundu:**

______________________________

(iii) Ife sitikufuna kusewera nanu.

**mtundu:**

______________________________

**(Malikisi 6)**

**4.** a. Perekani mitundu ya mifuwu yomwe ili ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

(i) Kani! Matapira ndi yemwe adaba nkhumba zanga.

______________________________

(ii) Chotsa zinyalala zako wataya apazi, asa!

______________________________

(iii) Mayo ine! Nyumba ija yapsa.

______________________________

(iv) Hehede! Mwana uja wandigulira galimoto.

______________________________

**(Malikisi 4)**

b. Perekani ntchito za nthambi zosaima pazokha zomwe zili ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

(i) Zomwe mwayankhula zadabwitsa anthu.

______________________________ **(Malikisi 1)**



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

(ii) Nkhosa imene yaphedwayo ndi ya a mfumu.

__________________________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) Awa ndi amene abwera.

__________________________________________ **(Malikisi 1)**

(iv) Chimwemwe akudya monga akuthawa.

__________________________________________ **(Malikisi 1)**

(v) Tikhale tcheru ku zomwe iyeyu ayankhule.

__________________________________________ **(Malikisi 1)**

(vi) Ndidzakhoza mayeso poti ndakonzekera bwino.

__________________________________________ **(Malikisi 1)**

## Gawo B (Malikisi 20)

### Kumvetsa Nkhani ndi Kusanthula Chiyankhulo

**5.** Werengani nkhani ili m'munsimu mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

Ine ndine Mtsimphina . Tsiku lina ndidapita kukachezera mnzanga wa nthanga imodzi dzina lake Gonerani, yemwe amakhala pa mudzi wa Chimonjo, ku tsidya lina la mtsinje wa Nakontho. Mnzangayu tidaphunzira limodzi ku sukulu ya sekondale yogonera komweko ya Kadyankena. Titamaliza maphunziro athu a m'kalasi lachinayi, tidayamba ulimi ngati ntchito yodzilemba tokha. Patapita zilumika zitatu, tonse tidapeza mphasa ngati wofuna kumafutsa mtambe, komanso popeza khasu la dzanja limodzi limapweteka. Mabanja athu adali osiririka ngati madzi a pambirira, koma timasiyana pa makhalidwe athu a pabanja.

Mwezi wathawu ndidaubutsa ulendo wopita kwa mnzangayo, kwa a Chimonjo, kukamuona. Nditafika, tidalonjerana mwansangala ngati agalu odziwana. Adandilandira kachingerengere kanga nakayedzeka m'shedi. Mnzangayu ndidamupeza ali pakalapakala ndi ana ake ngati nyerere. Aliyense adali kugwira ntchito yakeyake. Iyeyu adali kuchapa



Downloaded for ***FREE*** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

zovala za ana ang'onoang'ono pamene mnyamata wake, yemwe amati n'chisamba chake, adali m'khitchini kukonza nkhomaliro. Mkazi wake amatsukuluza zovala zimene Gonerani uja ankachapa. Izi zidali zondidabwitsa kwambiri. Ndidati mumtima mwanga: "Ngati m'mankhwala achikondi amene mnzangayu adadya, ndithu adamusandutsa chitserekwete. Mpaka kuchapa zovala za makanda? Kaninso akadalipo ana aamuna opusabe ngati nsima, masiku ano, oti n'kumaphika pa msinkhu wa zaka khumi ndi zisanu n'ziwiri zakubadwa, amayi awo ali pompo?" Amenewa adali maganizo anga omwe ndidasankha kuti akhale angaanga, ndisawatulutsire poyera. Ana awo aakazi ocheperapo msinkhu poyerekeza ndi mnyamatayo, ndiwo ankatunga madzi otsukuluzira zovala zija. Ine ndidapukusa mutu ngati ng'ombe yolumidwa ndi njuchi.

Atatha kukonza chakudyacho, mnyamatayo adachita zonse zofunika patebulo. Titadya, tidakakhala m'shedi muja n'kuyamba kucheza. Chifukwa chakuti timamwera chigoba chimodzi ngati mbalame za udzungulu, ndidafunsa chifukwa chimene Goneraniyo adazerezekera mpaka kumachapa zovala za ana nthiti yake ili pomwepo. Iye adandifotokozera kuti m'banja mwawomo adagwirizana kuti aliyense azitengako gawo pa ntchito zapakhomo, mosatengera kuti ndi wamwamuna kapena wamkazi. Ndidaseka chikhakhali mpaka mphafa kuwawa, misozi n'kutulukanso m'maso. Nditasiya kuseka kuja, ndidazizwa kuti mnzanga uja samaoneka kuti zamukhudza ayi. Ndekha ndididya mutu n'kuona kuti m'zokamba za mnzangayo mudali mfundo yabwino zedi.

Ndidatsanzika kuti ndione msana wanjira, koma adandiumiriza kugona komweko. Madzulo tidaswerana kasongo pokumbutsana za pa ubwana wathu tili kusekondale, ndi momwe tidapezera otisandutsa anthuanthuwa. M'mawa, idandidzutsa ndi nkhwangwa. Nditasuzumira pazenera, ndidaona kuti bambo am'nyumbamo, anzanga aja, ali kudumpha nayo nkhwangwa ngati waganyu. Kenako adalowa m'khitchini kukasonkha moto. Mwana wina wamkazi adali akusesa pomwe mnyamata uja ndi msungwana winanso ankatunga madzi kuchokera ku mjigo. Amayi am'nyumbamo adali kutsuka mbale. Nditatuluka m'chipinda m'mene ndidagonamo, ndidaona kuti pafupifupi chilichonse chidali chitakonzedwa kale. Ntchito zidapitirira ndipo anthuwa ankangokhala ngati a msinkhu umodzi. Mayi adakonza kadzutsa woti tonse tidye.



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Ndidadzimvera chisoni poganizira za kukhomo kwanga komwe ine ndimangokhala kusiya mkeka wanga ndi ana ntchito zikuwathyola ngati ine ndidapita kumsabwera. Ndekha ndidazindikira kuti kuthandizana ntchito zapakhomo ndi chinthu chaulemu zedi, popeza ntchitozo zimagwirika mwachangu komanso mosachita kudula nazo msana ngati wozula ziputu zakudimba. Ndidaonanso kuti kuthandizana kotere kungachititse anthu kukhala ndi mtima woyamikira ntchito za ena popeza aliyense amadziwa tanthauzo kapena kuwawa kwa ntchitoyo. Ndidaphunzirakonso kuti mgwirizano wotere umalimbikitsa ubale wabwino m'banja.

Ndidachokako kwa mnzanga uja nditaphunzira zambiri pa masiku awiri omwe ndidakhala kumeneko. N'tafika kwathu ndidaika banja langa pasukulu, maka pomupepesa mkazi wanga pa momwe ndimamugwiritsira ntchito zapakhomo ngati kapolo. Mkazi wangayu adati, "Ho! Ndiye khundabwi mwakadya kwa a Goneraniko ameneyu? Ayi, tiziona poti nyambo m'masiku. Lero nanga simuyambira mthiko kuti tidziwedi zoti munali ku chitsitsimutso cha ntchito zapabanja, ndipo mwatembenukadi? Mwina n'kutero kuti ng'ombe yanu yapajokine ndisalaleko." Ana athu ankangoseka chomwetulira uku akundipenyetsetsa tate wawone. Panopa aliyense adayamba kugwira ntchito mosaona kuti ndani m'banjamo.

**Mafunso**

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa momveka bwino.

a. Kodi Mtsimphina ndi Gonerani adadziwirana kuti?

..................................................................................................**(Malikisi 1)**

b. Ndi nthawi yanji imene Mtsimphina adafikira kwa a Chimonjo?

................................................................................................**(Malikisi 1)**

c. Fotokozani chomwe chidachititsa Mtsimphina kuti aganize zoti Gonerani adali chitsiru zedi.

.....................................................................................................................

..................................................................................................................

**(Malikisi 2)**



Downloaded for ***FREE*** from *www.kizitochikuni.com* - For more info: *contact@kizitochikuni.com*

d. Malinga ndi nkhaniyi, mukuganiza kuti papita zaka zingati abwenzi awiriwa atatsiriza maphunziro awo pa sekondale ya Kadyankena?

.....................................................................................................................

**(Malikisi 2)**

e. Ndi phunziro lalikulu liti lomwe Mtsimphina adatolapo pa kusaseka ndi kudekha mtima kwa Gonerani m'shedi muja?

.........................................................................................................................

.....................................................................................................................

**(Malikisi 2)**

**f.** Fotokozani ubwino womwe umadza ndi mgwirizano wa pa ntchito zapabanja.

.........................................................................................................................

.....................................................................................................................

**(Malikisi 2)**

g. Pezani chining'a m'nkhanimu chomwe tanthauzo lake ndi ili:

"Nthawi siikhalira kupita":

________________________________________________**(Malikisi 2)**

**b. Kusanthula Chiyankhulo**

i. Pezani zining'a m'nkhanimu zomwe matanthauzo ake ndi awa;

1. a misinkhu yofanana :

   ____________________________________________**(Malikisi 1)**

2. akazi omanga nawo banja:

   ____________________________________________**(Malikisi 1)**

3. tidakambirana zambiri zedi:

   ____________________________________________**(Malikisi 1)**

4. mkazi wanu wokugwirirani ntchitone:

   ____________________________________________**(Malikisi 1)**

ii. Kuchokera mu nkhaniyi pezani zifanifani zomwe matanthauzo ake ndi awa.

1. Tidakwatira kuti tizithandizika pa ntchito.

   ____________________________________________**(Malikisi 2)**



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**CANDIDATE NUMBER: ________________________________**

2. Ali kuwaza nkhuni molimbika kwabasi.

   ________________________________________________ **(Malikisi 2)**

## Gawo C (Malikisi 15)

### Chifupikitso

**6.** Werengani nkhani yotsatirayi mosamala. Ili ndi mawu ***163*** ndipo muifupikitse kuti ikhale ndi mawu osachepera **50** koma asapitirire **60.**

### KUSEFUKIRA KWA MADZI

Chaka ndi chaka mu nyengo ya mvula madzi amasefukira m'madera ambiri otsika kuno kwathu ku Malawi. Izi zimachitika ngakhale m'maiko ena. Makono kusefukiraku kukunka kukukulirakulirabe poyerekeza ndi zilumika zambiri zam'mbuyomu.

Madzi akasefukira, zinthu zambiri zimaonongeka. Ziweto monga mbuzi, ng'ombe, nkhuku ndi zina zimafa ndi madzi. Sizokhazi ayi, mbewu nazonso zimaonongeka. Kuonongeka kwa mbewu chotsatira chake ndi njala yomwe imavutitsa anthu. Nyumba nazonso zimagwa. Zikatero anthu ambiri amasowa pogona. Chifukwa cha kugwa kwa nyumbaku, katundu wambiri monga ziwiya, mipando ndi zina amaonongeka. Izi zimachititsa kuti anthu asowe mtengo wogwira.

Kusefukira kwa madziku kukukulirakulira masiku ano kaamba kodula mitengo mwachisawawa. Anthu akumadula mitengo pa zifukwa zosiyanasiyana m'mapiriwa ndiponso mphepete mwa mitsinje. Izi zikuchititsa kuti mapiriwa ndiponso mphepete mwa mitsinjemu mukhale mbulanda choncho mvula ikagwa palibe chomwe chimatha kuyimitsa madzi ayi. Zotsatira zake madziwo amakokolola nthaka imene imakagwera m'mitsinje. Zikatero ndiye kuti mitsinje imakwiririka, simakhalanso yakuya ayi. Chifukwa chochulukana, anthu ena amatsekula minda yawo m'mphepete mwa mistinje. Izinso zimachititsa kusefukira kwa madzi.



Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**CANDIDATE NUMBER:** ________________________________

________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________

## Gawo D (Malikisi 15)

### Chimasuliro

**7.** Masulirani nkhani yotsatirayi m'Chichewa chomveka bwino.

### EFFECTS OF CLIMATE CHANGE

Malawi is one of the most affected countries by climate change. This has negatively affected agricultural production which is the economic backbone of the country.

The impact of climate change in Malawi is being manifested in various ways. These are intense rainfall, floods and prolonged dry spells.

People are living in poverty because they depend on good rains for food. This poverty is now forcing some people to engage in immoral behaviour as a way of finding money for



*Downloaded for* ***FREE*** *from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com*

food. This puts them at risk of contracting HIV and AIDS and other sexually transmitted diseases.

**MAFUNSO ATHERA PANO!**

**NB: Pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi atatu.**



*Downloaded for* ***FREE*** *from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com*